

# ZIMENE MPINGO WA FOURSQUARE UMAKHULUPIRIRA



1. **Malemba Oyera** 2 Timoteo 3:16,17

Timakhulupirira kuti Baibulo ndi louziridwa ndi Mulungu.



2. **Utatu wamuyaya wa Mulungu** 1 Yohane 5:7

Timakhulupirira za utatu wamuyaya wa Mulungu; Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera.

3. **Kugwa kwa munthu** Aroma 5:12

Timakhulupirira kuti munthu analengedwa mchifanizo cha Mulungu mwini. Munthu analephera kukhala mu chiyanjano ndi Mulungu chifukwa cha kusamvera.



4. **Chikonzero cha Kuombedwa** Yohane 3:16

Timakhulupirira kuti pamene tinali ochimwabe, Khristu anatifera, kupereka chikhululukiwo kwa onse omkhulupirira Iye.

5. **Chipulumutso mwa chisomo** Aefeso 2:8

Timakhulupirira kuti sindife olungama koma tiyenera kubwera kwa Mulungu ndi kupempha kulungama kwa Khristu.



**6. Kulapa ndi kuvomerezedwa** 1 Yohane 1:9

Timakhulupirira kuti pamene tilapa moona mtima ndi kumulandira Khristu ndi mtima wonse, timalungamitsidwa ndi Mulungu.

**7. Kubadwanso mwatsopano** Yohane 3:3

Timakhulupirira kuti kusinthika kumene kumachitika mu mtima panthawi yotembenuka kumakhala kwenikweni.

**8. Moyo wa Chikristu wa tsiku ndi tsiku** Ahebri 6:1

Timakhulupirira kuti ndi chifuniro cha Mulungu kuti tikaretsedwe tsiku ndi tsiku ndi kukula m'chikhulupiriro.

**9. Ubatizo ndinso Mgonero wa Ambuye** Mateyu 28:19;

1 Akorinto 11:28

Timakhulupirira kuti ubatizo womizidwa m'madzi umaonetsera kunja ntchito imene yachitika mkati mwa munthu.

Timakhulupirira pa kukumbukira mgonero wa Ambuye pogwiritsa ntchito mkate ndi madzi a zipatso.

**10. Ubatizo wa Mzimu Woyera** Mchitidwe 2:4

Timakhulupirira kuti ubatizo wa Mzimu Woyera umampatsa wokhulupirira mphamvu zochitira umboni za Yesu ndinso kukhala moyowachigonjetso monga m'mene unabwerera masiku a m'Baibulo.

**11. Moyo wodzazidwa ndi Mzimu Woyera** Agalatiya 5:16,25

Timakhulupirira kuti ndi chifuniro cha Mulungu kuti tikayende mwa Mzimu tsiku ndi tsiku.

**12. Mphatso ndi chipatso cha Mzimu Woyera** 1 Akorinto 12:1-11;

Agalatiya 5:22

Timakhulupirira kuti Mzimu Woyera ali ndi mphatso zimene

umapereka kwa Mkhristu. Komanso kuti tikaonetse chipatso chauzimu kuti chikhale chizindikiro cha moyo wodzadzidwa ndi Mzimu Woyera.

**13. Chikatikati Afilipo 4:5**

Timakhulupirira kuti moyo watsikunditsiku wa wokhulupirira usamutsogolere ku mchitidwe wonyanira.

**14. Machiritso kudzera mu Mphamvu ya Mulungu Yakobo 5:14-16**

Timakhulupirira kuti machiritso kudzera mu mphamvu ya Mulungu ndiyo mphamvu ya Khristu yochiritsa wodwala kukhala yankho la pemphero la chikhulupiriro.

**15. Kubweranso kwa Yesu Khristu 1 Atesalonika 4:16,17**

Timakhulupirira kuti kubweranso kachiwiri kwa Yesu Khristu ndi zoonadi.

**16. Chiyanjano ndi Mpingo Machitidwe 16:5**

Timakhulupirira kuti ndi udindo wathu wopatulika kuti tikhale pa mpingo, kukhala membala wokhulupirika pa mpingopo.

**17. Boma la M'dziko Aroma 13:1-5**

Timakhulupirira kuti olamulira ayenerakumveredwa nthawi zonse kupatula pa zinthu zomwe ndi zotsutsana ndi chifuniro cha Mulungu.

**18. Chiweruzo Chomaliza 2 Akorinto 5:10**

Timakhulupirira kuti wina aliyense adzafika pa mpando wachiweruzo wa Mulungu ndipo adzalandira moyo wosatha kapena imfa.

**19. Kumwamba 1 Akorinto 2:9**

Timakhulupirira kuti Kumwamba ndi kunyumba kwa ulemelero wopambana ndipo ndi kwamuyaya kumene anthu okhulupirira ndi kubadwanso mwatsopano akakhale.

**20. Jehena Chivumbulutso 20:10,15**

Timakhulupirira kuti jehena ndi malo amazunzo komwe anthu amene amkana Yesu kuti si Mpulumutsi wawo akakhaleko mpaka muyaya.

**21. Kufalitsa Uthenga Wabwino Yakobo 5:20**

Timakhulupirira kuti kubweretsa anthu kwa Yesu ndi ntchito yopambana ya mpingo pano padziko lapansi.

**22. Zakhumi ndi zopereka Malaki 3:10; 2 Akorinto 9:7**

Timakhulupirira kuti zakhumi ndi zopereka ndi njira yoikidwa ndi Mulungu yothandizira kufalitsa Mau ake.

Mau oti “Foursquare” akuimirira utumiki unayi wa Yesu Khristu monga Mpulumutsi (Aroma 10:9), Mbatizi wa Mzimu Woyera (Luka 3:16), Mchiritisi (1 Petro 2:24), ndi Mfumu imene ikubwera (Machitidwe 1:11).